Kodi Yesu Khristu Ndi Ndani? (Gawo 3)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 4 m'buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI YESU ANALI MUNTHU WOTANI?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi mukuganiza kuti anthu ena angayankhe bwanji?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Yesu anali ndi makhalidwe ofanana ndendende ndi Yehova Mulungu, yemwe ndi Atate ake.
(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 15 mpaka 19.)

Werengani Yohane 14:9.
Kodi Yesu ankatanthauza chiyani pamene ananena kuti: "Amene waona ine waonanso Atate"?

Werengani Mateyu 9:35, 36; 21:12, 13; Maliko 10:13-16.
Kodi Yesu anasonyeza bwanji kuti anali munthu wolimba mtima komanso wachifundo?



Zimene Yesu ankachita ndi kunena zinasonyeza mmene Atate ake amaganizira komanso mmene amamvera

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Yesu anali wokhulupirika.

(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 20.)

Werengani Mateyu 4:1-11.

Kodi zomwe Yesu anachita posagonja pamene Satana ankamuyesa, zinasonyeza bwanji kuti anali wokhulupirika kwa Mulungu?

Yesu anali wokhulupirika.

(Werengani mutu 4 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 21-22.)

Werengani Afilipi 2:8.

N'chifukwa chiyani Yesu anafunika kukhala wodzichepetsa kuti achite zonse zimene Mulungu anamuuza?

Kodi ndi makhalidwe ati a Yesu amene amakusangalatsani kwambiri?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

N’zosatheka kudziwa kuti Mulungu ndi wotani chifukwa palibe amene anamuonapo.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N’zoona kuti palibe amene anaonapo Mulungu. Koma ndimakhulupirira kuti Yesu angatiphunzitse bwino kwambiri zokhudza Mulungu chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Yesu sanali wolimba mtima chifukwa ankangonena zokhudza chifundo ndi chikondi.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Anthu ambiri angavomereze zimene mukunenazo. Koma ine sindikhulupirira zimenezo chifukwa. . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania